Coptic Orthodox Patriarchate
His Holiness Pope Tawadros II
Pope of Alexandria and
Patriarch of the See of St. Mark
The Papal Center

222 Ramses St., Abbaseya, Cairo, Egypt
Tel: 024822580 Fax: 0235365880 email: office@popetawadros.org

بطريركية الأقباط الأرثوذكس
قداسة البابا الأنبا تواضروس الثاني
بابا الأسكندرية
وبطريرك الكرازة المرقسية
المقر البابوي

222 شارع رمسيس ، العباسية ، القاهرة ، مصر
تليفون: 024822580 فاكس: 0235365880

Chichewa – Resurrection 2025

Dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Oyera, Mulungu M'modzi, men.

Ekhristos Anesti, Elithous Anesti. Khristu wauka. Zowonadi wauka

Ndikupatsani mafuno abwino nonse pa chikondwerero ichi cha kuwuka kwa Ulemu. Chikondwerero chomwe tikumalizitsa nyengo ya kusala koyera komwe kwatenga masiku 55. Tikhala tikukondwerera kwa masiku ena okwana 50 kutsogoloku, omwe tikuwatchula Masiku 50 Oyera.

Mu chikondwerero cha Ulemu cha kuwuka, timakondwerera ntchito ya Mulungu pa lfe, pamene iye akutipatsa ife madalitso ochuluka. Anatipatsa ife chikondi, chisomo komanso umodzi ndi Iye. Izi ndi zomwe ife timakhala tikunena pa mapeto a mapemphero athu nthawi zonse. Timanena kuti chikondi cha Mulungu Atate, chisomo cha Mwana M'modzi Wake Yekhayo, limodzi ndi mphatso za Mzimu Oyera. Madalitso atatu amenewa tinalandira mu kuwuka kwake kwa Ulemu, kapena tinene kuti chifukwa cha kuwuka kwake kwa Ulemu.

Choyamba, chikondi chomwe Mulungu anatikonda nacho, chifukwa choti anabwera pa dziko lapansi chifukwa chotikonda. Timamukonda chifukwa choti koyamba Iye anatikonda(1 John 4:19). Uku kunali kubadwa kwake kwa Ulemu. Kubadwa kwa ulemu kwa Mulungu ndiyo njira yomwe Iye anadzera kufikira pa dziko lapansi. Chikondi chake si cha nkhamba kamwa chabe, mawu chabe, kapena chapatali, koma ndi chikondi chenicheni. Anabwera ndipo anabadwa, ndipo mawu anasandulika munthu nakhala pakati pathu ndipo tinaona Ulemelero wake (John 1:14). Umu ndimo Mulungu anakondera dziko la pansi. Palibe chikondi chomwe chingakhale chopambana kapena cha mphamvu ngati kukhala naye pafupi wokondedwa wako. Aliyense mwa ife anakhala wokondedwa wa Mulungu.

Chachiwiri ndiye chisomo: Chisomo cha kuwuka, chisomo cha kukhululukidwa machimo, chisomo cha kuwomboledwa, chisomo cha kudzisanthula. Tinalandira chisomo chimenechi kupyolera mu ntchito ya Khristu. Kubadwa kwake kwa pa dziko, kenako kufa kwake kwa pa mtanda chifukwa cha ife. Kenako kuwuka kwake kwa

chipulumutso chathu. Chisomo cha chikulu chimenechi chimampatsa munthu chisomo cha kuwuka kwa akufa. Monga tikudziwa kuti kuwuka ndiko "kudzuka," ntchito ya mphamvu. Munthu amene anakhala pansi ndiye nkuwelamuka kenako nkuyimirira. Ichi ndi chizindikiro cha kukonzekera, ndipo chizindikiro choti munthu ali ndi umoyo wathanzi: Kudzuka. Choncho, timayimba nyimbo ya matamando ya tsiku ndi tsiku kuti: Dzukani inu ana a kuwala, tiyeni titamande Ambuye a Makamu. Ana a kuwala ndi ana a kuwuka. Ndipo timayamba ndi mneni kuti, "Dzukani" Ichi ndiye kuwuka kwa ulemu komwe ife timapeza.

Komanso, kukhala limodzi ndi Mzimu Oyera, amene amatilumikizitsa tonse mu mpingo umodzi, mu chikhulupiriro chimodzi, mu ntchito imodzi, mu chiyembekezo chimodzi, komanso kuyamba ndi chikondi chimodzi. Tonse timakhala amodzi mu thupi la Khristu. Ndipo Mzimu Oyera mwa ife amatilumikizitsa tonse kupyolera mu masakaramenti, kupyolera m'mapemphero, kupyolera mu kuwerenga, ndi zonse zochitika za uzimu.

Ichi ndi chikondi, chisomo, ndinso umodzi. Choncho, pemphero lililonse, wansembe amamaliza ndi mau amenewo. Amatikumbutsa za ntchito ya Mulungu pa ife ya chikondi, chisomo, ndi umodzi wathu ndi Iye. Iyi ndiye ndondomeko yathu ya Mau owerengedwa mu Church. Izi zikupezeka mu Mau a Mnthenga wabwino owerengedwa nthawi ya chipembedzo mu chaka chonse cha Chi Coptic. Mu miyezi ya Tut ndi Babah, timaphunzira za chikondi cha Mulungu. Mu miyezi khumi ndi iwiri yotsatira yake kuyambira mwazi wa Hathor, timaphunzira za chisomo cha Mwana wake M'modzi yekhayo, amene anakhala ndi ife. Kenako pa miyezi yotsalayo timaphunzira za umodzi wathu ndi Iye, luso,ndi mphatso za Mzimu Oyera.

Kuwuka ndiye mphamvu yayikulu zedi. Nkhani ya pamwamba zedi yabwino yomwe imafaniziridwa ndi kuwuka ndi iyi: Ana ena anafunsa moto, "kodi iwe ndi chinthu cha mphamvu zedi pa dziko la pansi?" Unawankha kuti, "Ayi, madzi ndiye amphamvu kuposa ine." Ndiye anapita kukafusa madzi, "Kodi iwe ndi chinthu cha mphamvu zedi pa dziko la pansi?" Unawawuza kuti, "Ayi, dzuwa ndiye lamphamvu kuposa ine. Limandisungunula ine." Anapita kwa Dzuwa, "Kodi ndiwe chinthu cha mphamvu zedi pa dziko la pansi?" Linawawuza kuti, "Ayi, mitambo imandiphimba." Ndiye anapita kwa mtambo nakawufunsa, "Kodi ndiwe chinthu cha mphamvu pa dziko la pansi?" Unawayankha kuti, "Ayi, mphepo imandisuntha kuchoka apa ndi apo." Ndiye anapita kwa mphepo mkukafusa, "Kodi ndiwe chinthu cha mphamvu pa dziko lonse lapansi?" Inayankha kuti, "Ayi, Phiri ndiye la mphamvu kuposa ine," chifukwa ndikamayenda Phiri limanditchingira ndipo sindingathe kudutsa," Ndiye anapita kwa Phiri ndikukafusa, ''Kodi ndiwe chinthu cha cha mphamvu pa dziko lonse la pansi?" Linawankha kuti, "Ayi, munthu ndiye ali wa mphamvu kuposa ine, chifukwa amatha

kundisalaza." Ndiye anapita kwa munthu nakafunsa, "Kodi ndiwe wa mphamvu pa dziko la pansi?" "Ayi, imfa ndiye ya mphamvu kuposa ine. Sindingagonjetse imfa." Ndipo anati, "Tiyeni tifunse imfa." "Kodi ndiwe chinthu cha mphamvu kwambiri?" Inawauza kuti, "Ayi, Khristu ndiye wamphamvu chifukwa anagonjetsa imfa. Monga momwe Mtumwi Paulo amatiphunzitsira: kodi imfa kupambana kwako kuli kuti? Iwe imfa ululu wako uli kuti? (1 Akorinto 15:55). Khristu anafa pa mtanda ndipo anawuka kwa akufa kuti agonjetse imfa. Chifukwa cha ichi, ife tiri ndi moyo wosatha. "Khristu anawuka kwa akufa." Kupyolera mu imfa, Wagonjetsa imfa, ndipo iwo amene ali m'manda anawapatsa moyo wosatha.

Mafuno abwino kwa inu nonse pa chikondwerero cha kuwuka kwa ulemu. Ndikufunirani mafuno abwino inu nonse ma Metropolitan, ma Bishop, ansembe, ma Hegomeni, ndi ma presibiteri. Mafuno abwino inu ma Dikoni ndi ma Archons. Mafuno abwino inu azitumiki, ndi mawanja onse a chi Coptic omwe lero akusangalalanso chifukwa cha kuwuka kwa ulemu. Mafuno a bwino kwa achinyamata onse ku ma tchalitchi onse, m'ma utumiki onse, ndi mbali zonse za dziko. Chosangalatsa kwambiri chaka chino ndi choti tikupanga chikondwerero chimenechi limodzi ndi ena onse. Akhristu onse pa dziko lonse akupanga chikondwerero chimenechi cha kuwuka tsiku limodzi. Ichi ndi chinthu cha bwino zedi. Chaka Chinonso tikuchita chaka cha 17th century chipangireni mkumano wa ukulu woyamba wa Ecumenical council wa ku Nicaea. Uwu ndi mkumano omwe unakambirana ndi kukhazikitsa chikhulupiriro cha akhristu: "Zowona ife tikhulupirira Mulungu m'modzi." Ndikufunirani mafuno abwino inu mipingo yonse ya pa dziko la pansi. Mafuno abwino kwa onse ogwira ntchito ndi otumikira. Ndikupereka uthenga wa chikondi kuchokera ku likulu la mpingo ku Egypt. Mipingo yathu yonse ya ku madzulo kwa America, ku m'mawa kwa America. Muno mu Africa, mpingo wa ku Yerusalemu, ku Asia, komanso ku Australia. Mafuno abwino apite kwa onse. Ndikufunirani chaka chopambana ndi kuwuka naye Khristu. Ndipo mukhale osangalala mu nthawi yonse ya moyo wanu. Koma tisaiwale chikondi, chisomo, komanso umodzi ndi Iye. Kwa Mulungu wathu kukhale ulemerero ndi ulemu, tsopano ndi kunthawi zonse. Amen.

Pawadros II